

Dziwani kuti: Nkhuku imodzi yayikulu imafunika malo okula masentimita 30 mbali zonse, kukula kwa khola kumatengera kuchuluka kwa nkhuku zomwe mlimi alinazo.

KAMANGIDWE KA KHOLA LA MBUZI

- Mangani khola la mbuzi pogwiritsa ntchito mitengo, matabwa, zipapati kapena nsungwi
- Gwiritsani ntchito mitengo yolimba pomanga khola kuti ikhale nthawi yayitali isanaonongeke komanso kuti mbuzi zisajiwe
- Khola litalike mita imodzi kuchoka pansi.

- Paphaka la khola pakhale mipata yoti ndowe zizigwera pansi. Onetsetsani kuti mipatayi ndi yocheperapo kuti mbuzi zisamalowetsepo miyendo ndi kuchita ngozi
- Konzani malo odyera mbuzi m'kholamo

Dziwani kuti: Khola lokula mamita atatu mulitali ndi mamita awiri mulifupi limakwana mbuzi khumi, pomwe khola lokula mamita anayi mulitali ndi mamita atatu mulifupi limakwana mbuzi mpaka makumi awiri.

MAU OMALIZA

Ulimi wa nkhuku za chiMalawi ndi mbuzi ndi opindulitsa. Alimi m'dziko muno akulimbikitsidwa kuweta ziwetozi kuti athane ndi mavuto obwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo. Kuti alimi apeze phindu lochuluka kuchokera ku ulimiwu, ayenera kumanga makola amakono.

Mukafuna kudziwa zambiri za makola a makono a nkhuku ndi mbuzi, kafunseni alangizi a ziweto kapena a za malimidwe omwe ali m'dera lanu.

Designed and Printed by
Agricultural Communication Branch
P.O. Box 594
Lilongwe

© 2019

IFAD
Investing in rural people

MAKOLA AMAKONO A NKHUKU ZA CHIMALAWI NDI MBUZI



Ulimi wa nkhuku za chiMalawi ndi mbuzi ndiopindulitsa chifukwa zimapilira ku chilala, sizifuna zakudya zambiri, komanso sizivuta kusamala.

UBWINO OWETA NKHUKU ZA CHIMALAWI NDI MBUZI

- Zimatipatsa nyama imene ili ndi michere yofunika mthupi
- Zimatipatsa ndalama tikagulitsa
- Zimatipatsa manyowa
- Mbuzi zimatipatsa mkaka ndipo nkhuku zimatipatsa mazira.
- Zimapilira ku chilala.
- Ulimi wa mbuzi ndi opindulitsa chifukwa zimatha kubereka katatu pazaka ziwiri komanso zimatha kubeleka ana awiriawiri
- Ulimi wa nkhuku ndi opindulitsa chifukwa zimaswana nsanga komanso zimaswa katatu ngakhale kanayi pa chaka.

Kuti mupindule ndi ulimi wa nkhuku za chiMalawi ndi mbuzi sungani ziwetozo m'makola omangidwa mwa makono.

UBWINO WA MAKOLA A MAKONO

- Ziweto zimatetezedwa ku nyengo yotentha, mvula komanso mphepo
- Ziweto zimatetezedwa ku matenda
- Ziweto zimakhala m'malo a ukhondo
- Ziweto zimatetezedwa ku akuba komanso nyama zolusa
- Kuyendera ziweto sikukhala kovuta
- Manyowa amachotsedwa mosavuta

MALO ABWINO OMANGA KHOLA

- Khola limangidwe pamalo o k w e r a kuti musamalowe madzi a mvula.
- Khola liyandikane ndi nyumba kuti ziweto zitetezedwe.

MITUNDU YA MAKOLA

- Khola la makono la mbuzi limayenera kukhala lam'mwamba
- Khola la makono la nkhuku limayenera kukhala lam'musi

KAMANGIDWE KA KHOLA LA NKHUKU

- Mbali zazitali za Khola ziyenera kuyang'ana kum'mawa ndi kumadzulo kuti musamalowe dzuwa lambiri
- Khola likhale lotalika mamita awiri kuchoka pansi kuti munthu athe kulowamo choyenda osati chogwada.
- Khola likhale ndi ngalande zochotsera madzi kuzungulira kholalo.
- Denga la nkhuku likhale lam'mwamba pafupifupi theka koma lomangidwa motsetsereka kuti muzikhala mthunzi komanso lisamadonthe
- Khola likhale ndi mazenera kuti muzilowa mpweya komanso kuti musamakhale fungo loyipa



- Ikani mabokosi m'khola kuti nkhuku ziziikiramo mazira.

- Ikani utuchi, udzu oduladula, zidutswa za makoko a chimanga kapena deya wa mpunga pansi pakhola kuti musamavutike kukonzamo komanso kuti musamakhale fumbi
- Konzani malo oti nkhuku zizipumirapo mkati mwakhola